# KUDZITETEZA KUCHIWEWE

## Mafunso ndi mayankho okhudza chiwewe




A nthambi yowona zamaphunziro mu Worldwide Veterinary Service akuthokoza mabungwe a International Rabies Taskforce, MSD Animal Health, ndi nthambi yowona zaziweto mu Unduna wa Zamalimidwe mudziko lino la Malawi pachithandizo chimene apereka kuti a Mission Rabies akathe kusindikiza kabukhuka

## KODI CHIWEWE NDICHANI?
Chiwewe ndi matenda amene amayambitsidwa ndi kachilombo kamene kamapezeka mu nyama zimene zimayamwa kapena kuyamwitsa (nyama zokhala ndi mabere). Kachilomboka kakalowa mthupi lanyamayi, kamakamatilira pa misempha ya nyama, nkuyamba kuswana, kenaka, kamayenda pang'onopang'ono kudzera mumisempha muja, ulendo wakuubongo wa nyamayo.

Zizindikiro zoyamba zamatenda a chiwewe ndi kupweteka kwa mutu ndi kutentha thupi; zizindikiro zoti munthu atha kuganiza kuti ali ndi chimfine. Kachilombo kakakafika kuubongo, zizindikiro zenizeni za matenda achiwewe zimayamba. Panthawiyi, palibenso chithandizo chimene wodwala atha kupatsidwa mpaka kuchira.

Pali mitundu iwiri ya chiwewe:

- **Chiwewe chaukali** – chinyama chimaonetsa mkhalidwe waukali kuphatikizira kulumaluma zinthu, misala, kutentha thupi, kutuluka thukuta, kudana ndi madzi, kukha dovu mosalekeza, komanso kulephera kugona.
- **Chiwewe chopusa** – minyewa imafooka, chinyama chimakanika kuzindikira zinthu, komanso ziwalo zimafa.

## KODI CHIWEWE NDICHOOPYSA KWA MUNTHU?
Chiwewe ndichoopysa kwambiri nthawi zonse ngakhale chilinso chopeweka kwambiri. Kachilombo kakangolowa muubongo, munthu, ngakhale chinyama chinachilichonse, amayamba zizindikiro zachiwewe. Kachilombo kamakaononga malo osiyanasiyana muubongo wamunthu, kasokoneza kayendedwe kabwino kathupi ndipo pang'ono ndi pang'ono, mtima kapena mapapo zimasiya kugwira ntchito ndipo munthu amamwalira.

## KODI NDINGACHITENGE BWANJI CHIWEWE?
Matenda a chiwewe amafala kudzera mmalovu a chinyama chomwe chili ndi kachilombo koyambitsa matendawa.

Munthu atha kutenga kachilombokа kudzera mu:
- Kulumidwa ndi chinyama chachiwewe
- Kunyambitidwa pachilonda/bala ndi chinyama chachiwewe
- Kukandidwa ndi zala zachinyama chachiwewe
- Malovu a chinyama chachiwewe kugwera mu maso, mumphuno kapena mukamwa.

## KODI NDINGATANI PAMENE NDIKUKAYIKIRA KUTI NDATENGA KACHILOMBO KACHIWEWE?
Pamene pali chikayiko kuti mwina munthu watenga kachilombo ka chiwewe kudzera mu kulumidwa, kunyambitidwa pa bala, kapena kukandidwa, ndibwino kupereka chithandizo choyamba nthawi yomweyo.

Chitani izi:

1. Tsukani pachilonda/pabala ndi sopo ndi madzi (mosabwereza madziwo) kwamphindi 15
2. Thirani pachilonda mankhwala a Iodine, Dettol, methylated spirit
3. Musamangepo pachilonda
4. Auzeni alangizi azaziweto amene ali mdera lanu. Amenewa ndiamene atha kudziwa ngati galu wakulumaniyo ali wobayitsa katemera wachiwewe kapena ayi
5. Pitani kuchipatala kuti mukalandire thandizo. Ngati akuchipatala anena kuti ndipoyenera kuti mulandire katemera wa chiwewe, chonde, wonesetsani kuti mwalandira katemera yense mwandondomeko yake.

## KODI NDINGADZIWE BWANJI KUTI GALU ALI NDI CHIWEWE?
Nyama yachiwewe imaonetsa zizindikiro izi:
- Kulephera kukhala malo amodzi
- Kuyesera kulumaluma zinthu zosaoneka ndi maso
- Kuthamangathamanga kopanda pake
- Kulumaluma zinthu

- Kuchucha malovu ambiri mosalekeza
- Kukhala ndiukali pamene chinyamacho sichinaputidwe
- Kuyenda mwadzandidzandi ngati woledzera
- Kufa ziwalo
- Kulephera kumeza zinthu
- Kudana ndi madzi

### KODI NDINGATANI PAMENE GALU AKUWONETSA ZIZINDIKIRO ZAMATENDA A CHIWEWE?

Musamuyandikire galu kapena kufuna kumugwira kuti mumumange, ndipo musachite china chilichonse choti chitha kumupweteka galu woteroyo. Zimenezi zitha kuyika moyo wanu pachiopysezo chachikulu.

Nthawi yomweyo imbani phone mwaulele ku Mission Rabies pa **3434** pamene mutauzidwe zoyenera kuchita. Chonde, muyesetse kuti mukhale mukukumbukira malo amene galuyo waonedwa, maonekedwe ake, komanso zinthu zokaikitsa zimene galuyo munamuona akupanga.

### KODI AGALU AMALANKHULA?

Inde, agalu amalankhula koma osati ndi mau mmene anthu amachitira. Ngati anthu, tikuyenera tikhale odekha tikakhala ndi agalu kuti tiphunzire chilankhulo chawo ndi kumawamvetsetsa akamalankhula.

Ngati anthu titha kamalankhulana nawo agalu athu ndipo atha kumatimva zimene tikuwauza.

Nthawi zambiri, agalu athu amapezeka kuti ali osangalala, amantha, kapena aukali (olusa). Ndichinthu chofunika kwambiri kuti ngati anthu tizitha kudziwa ngati galu wathu ali wamantha, wansangala kapena waukala kuti tikathe kudziwa mmene tingachezere naye.

- **Galu wosangalala** – amayendetsa mchira wake mwapang'onopang'ono, komanso amatsegula kukamwa kwake koma osaonetsa mano ake.
- **Galu wamantha** – amapindira mchira wake pakati pamiyendo yake yakumbuyo, makutu ake amawagoneka pansi ndipo amayesetsa kuti alichepetse thupi lake ngati kufuna kulowa pansi.
- **Galu olusa** – amatsegula kukamwa kwake nkumaonetsa mano ake moopyseza, amauwa moopyseza, mchira wake umayima osagwedera.

Nthawi zonse tiyesetse kupewa kuyandikira galu wamantha komanso olusa kupewa kulumidwa.

### NDINGADZITETEZE BWANJI KUTI NDISALUMIDWE NDI AGALU?

Chachikulu tikakhala ndi galu tizimupatsa ulemu komanso tisamapange zinthu zoti zithe kumukwiyitsa kapena kudzetsa mantha pa iye.

Tikakumana ndi galu wachilendo, zina zofunika kuchita ndi izi :

- Ngati ali patali… yendani mofatsa ndipo mupite pamalo poti sangakulumeni ngati kulowa mnyumba, kusintha njira.
- Ngati galu akubwera kumene inu muli… kwerani pamwamba pachinthu ngati papilala, mumtengo. Ngati muli ndi chinthu mmanja choti mutha kuyika pakati pa galu ndi inu, chiyikeni ndithu.
- Ngati galu wakuyandikirani kwambiri kuti palibe chomwe mutha kuchita… imani njoo ngati mtengo manja anu mutawapindira pachifuwa panu. Musasunthe ndipo musamuyang'anenso galu mmaso. Yang'anani kumbali.

### NANGA NDINGATANI NGATI GALU AKUFUNA KUNDILUMA?

Imani njoo ngati mtengo manja anu mutawapindira pachifuwa panu. Ngati galu wakugwetserani pansi, dzipindeni/dzikulungeni ngati mwala ndipo gwiritsani nthito manja anu kuti galu asakulumeni kumutu kapena mukhosi.

Kudzipinda/kudzikulunga ngati mwala kumathandiza kuti galu asakulumeni kumutu kapena mukhosi. Ndibwino kuti galu akulumeni mmanja kapena mumiyendo kusiyana ndi kumutu

kapena mukhosi chifukwa ndichapafupi kuti kachilombo ka chiwewe kalowe muubongo wanu ngati mwalumidwa kumutu kapena mukhosi kusiyana ndi kulumidwa pamwendo pamene patenge masiku ochulukirapo kuti kachilombo kakafike kuubongo. Panthawiyi, mukhala muli ndi mwayi wolandira katemera wachiwewe.

### KODI ANA AZIWOPA AGALU?

Ayi. Ana asamaope agalu makamaka ngati agalu ali osangalala. Ana asamachite mkhalidwe umene utha kupangitsa galu kuti achoke posangalala nkusanduka wamantha kapena olusa. Mkhalidwe wogenda agalu, kuwazunza, kuwasokoneza akamadya, akamagona, kapena akakhala ndi ana utha kukwiyitsa galu, mmene munthunso atha kukwiyira.

### KODI ANTHU AMATETEZEKA BWANJI KU CHIWEWE KUDZERA MUKATEMERA WA AGALU?

Agalu amafalitsa chiwewe popatsirana komanso popatsira anthu ndi nyama zina. Chiwewe chopezeka mwa anthu, kwambiri chimachokera kwa agalu chifukwa anthu ndi agalu amakhalira limodzi kwambiri.

Nthawi zonse tikumbukire kuti siagalu onse ali ndi kachilombo koyambitsa chiwewe, koma tiyeni titenge kulumidwa ndi galu kwina kuli konse ngati chiopyezo choti wolumidwa uja atha kutenga kachilombo kachiwewe. Ndichinthu chofunikira kwambiri kupereka chithandizo choyamba munthu akalumidwa ndi galu nthawi zonse asanathamangire kuchipatala.

Kupereka katemera wa chiwewe kwa anthu ndikodula kwambiri. Kupereka katemera wachiwewe kwa agalu ndikotchipirako. Galu amafunika jakisoni mmodzi yekha kuti atetezeke kuchiwewe kwachaka chonse chathunthu pamene munthu amafunika majakisoni angapo akalumidwa ndi galu. Katemerayu ndiodula kwambiri.

### OSAPEREKA KATEMERA WA CHIWEWE KWA ANTHU BWANJI MMALO MWA AGALU?

Kupereka katemera wachiwewe kwa anthu ndikodula kwambiri kuyerekeze ndi kupereka katemerayu kwa agalu. Bungwe loona zaumoyo padziko lapansi la World Health Organisation (WHO) limapereka upangiri wonena kuti ngati agalu 7 pa agalu 10 (70%) alandira katemera wa chiwewe mdera, tikhala tikuchepetsa kufala kwa kachilombo ka chiwewe kudzera mwa agalu.

### KODI KATEMERA WACHIWEWE NDIOOPYSA KWA GALU WANGA?

Ayi. Katemerayu ndiwabwino kwa agalu onse; tiana, akuluakulu, komanso agalu oti ali ndi bere. Ngakhale katemera ameneyu amateteza agalu ku chiwewe, tidziwe kuti sateteza agalu ku matenda ena amenenso atha kudzetsa imfa kwa agalu.

### KODI KATEMERA WACHIWEWE AMAPEREKEDWA KANGATI PAMOYO WA AGALU?

Katemerayu amaperekedwa kamodzi pachaka kwa galu wina aliyense. Izi zikutanthauza kuti galu wina aliyense akuyenera kulandira katemerayu chaka chilichonse.

Katemerayu amapezeka kwa alangizi a ziweto ndi kwa mabungwe ena amene amayang'anira zinyama. A Mission rabies amapereka katemerayu mwaulele.

### NDIKUFUNA NDITADZIWA ZAMBIRI ZA CHIWEWE, NDINGAPITE KUTI?

Pitani pa masamba awa apa intaneti:

**www.malawi.missionrabies.com/en/education**

**www.wvsacademy kapena pangani scan QR code iyi:**

**www.missionrabies.com/en/education**

**www.who.int/health-topics/rabies#tab=tab_1**

MISSION RABIES

World Health Organization

WVS MALAWI